The Fear of the Lord

Kuopa Yehova ndiko korona wanzeru, wakukulitsa mtendere ndi thanzi langwiro; zonse zomwe ziri mphatso za Mulungu; Muzu wa nzeru ndiwo kuopa Yehova, Ndi nthambi zace ndi moyo wautali. MLALIKI 1:18,20

Tapenyani mibadwo yakale, nimuone; Kodi adakhulupirira Yehova, nachitidwa manyazi? Kapena kodi wina anakhalabe m'kuopa kwake, nasiyidwa? Kapena adapeputsa ndani amene adamuyitana? Iwo akuopa Yehova sadzaphwanya Mau ake; ndipo iwo akumkonda adzasunga njira zake. Iwo akuopa Yehova adzafunafuna chokoma, chomkondweretsa; ndipo iwo akumkonda Iye adzadzazidwa ndi lamulo. Iwo akuopa Yehova adzakonza mitima yawo, nadzadzichepetsa pamaso pake; Kuti, Tidzagwa m'manja a Yehova, si m'manja a antu : kuti monga kupambana kwatshi kuli, tshointsho tshointsho tshatshi.
MLALIKI 2:10,15-18

Kuopa Yehova kutsogoza kulandira ulamuliro; Amuna akulu, ndi oweruza, ndi amphamvu, adzalemekezedwa; koma palibe wina wa iwo wamkulu woposa iye wakuopa Yehova. MLALIKI 10:21,24

Ndipo usaope, mwana wanga, kuti tasauka; pakuti uli ndi cuma cambiri, ukaopa Mulungu, ndi kupatuka ku zoipa zonse, ndi kucita comkondweretsa pamaso pake. TOBI 4:21

Koma muziopa Yehova, ndi kumtumikira m'coonadi ndi mtima wanu wonse; 1 SAMUELE 12:24

Nanga nzeru ichokera kuti? ndipo malo a luntha ali kuti?
Ndipo kwa munthu anati, Taonani, kuopa Yehova ndiko nzeru; ndipo kupatuka pa choipa ndiko luntha. YOBU 28:20,28

Kuopa Yehova kuli koyera, kosatha; maweruzo a Yehova ali oona ndi olungama onse. SALIMO 19:9

Dziko lonse lapansi liope Yehova; SALIMO 33:8

Opani Yehova, inu okondedwa ake; Idzani, ana inu, mundimvere ine: Ndidzakuphunzitsani kuopa Yehova. Ndani munthu wofuna moyo, nakonda masiku ambiri, kuti aone zabwino? Uletse lilime lako ku zoipa, ndi milomo yako kusalankhula chinyengo.
Choka zoipa, nuchite zabwino; funa mtendere, nuutsate.
SALIMO 34:9, 11-14

Kuopa Yehova ndiko chiyambi cha nzeru: Onse akuchita malamulo ake ali ndi luntha labwino; SALIMO 111:10

Inu akuopa Yehova, khulupirirani Yehova: Iye ndiye mthandizi wao ndi chikopa chawo. Adzadalitsa iwo akuopa Yehova, ang'ono ndi akulu. SALIMO 115:11, 13

Anene tsopano iwo akuopa Yehova, kuti chifundo chake amakhala kosatha. SALIMO 118:4

Ngakhale wocimwa acita coipa kakhumi, natalikira masiku, koma ndidziwa ndithu kuti cidzakhala bwino kwa iwo akuopa Mulungu, akuopa pamaso pake; Koma woipa sadzakhala bwino, ndipo sadzatalikitsa masiku ake, amene ali ngati mthunzi; chifukwa saopa pamaso pa Mulungu. MLALIKI 8:12-13

Timve mathedwe a nkhani yonse: Opa Mulungu, sungani malamulo ake: pakuti iyi ndiyo ntchito yonse ya munthu.
Pakuti Mulungu adzaweruza ntchito iliyonse, ndi zobisika zonse, kaya zili zabwino kapena zoipa. MLALIKI 12:13-14

Yehova ndiye wokwezeka; pakuti akhala m'mwamba, wadzaza Ziyoni ndi ciweruzo ndi cilungamo. Ndipo nzeru ndi kudziwa kudzakhala kukhazikika kwa nthawi zako, ndi mphamvu ya chipulumutso; kuopa Yehova ndiko chuma chake. YESAYA 33:5-6

Lemekezani anthu onse. Kondani ubale. Opani Mulungu.
Lemekezani mfumu. 1 PETRO 2:17

ndi kunena ndi mau akuru, Opani Mulungu, mpatseni ulemerero; pakuti yafika nthawi ya chiweruzo chake;
CHIVUMBULUTSO 14:7

Kuopa Yehova ndiko chiyambi cha kudziwa: koma opusa anyoza nzeru ndi mwambo. MIYAMBO 1:7

Usakhale wanzeru pamaso pako; opa Yehova, nupewe zoipa.
Zidzakhala zochiritsa mchombo wako, ndi mafuta a mafupa ako.
Miyambo 3:7-8
Kuopa Yehova ndiko kuda zoipa; kunyada, ndi kudzikuza, ndi njira yoipa, ndi m'kamwa mopotoka, ndidana nazo.
Miyambo 8:13

Kuopa Yehova ndiko chiyambi cha nzeru: kudziwa woyera mtima ndiko luntha. Miyambo 9:10

Kuopa Yehova kumatalikitsa masiku; Koma zaka za oipa zidzafupikitsidwa. MIYAMBO 10:27

M'kuopa Yehova muli chikhulupiriro cholimba, ndipo ana ake adzakhala ndi pothawirapo. Kuopa Yehova ndiye kasupe wa moyo, Kucoka ku misampha ya imfa. MIYAMBO 14:26-27

Zochepa uli ndi kuopa Yehova zipambana ndi chuma chambiri ndi mavuto. Kuopa Yehova ndiko mwambo wanzeru; ndipo patsogolo ulemu ndi kudzichepetsa. Miyambo 15:16, 33

Ndi cifundo ndi coonadi mphulupulu zitsukidwa; Miyambo 16:6

Kuopa Yehova ndiko kutsata moyo; sadzalangidwa ndi choipa. MIYAMBO 19:23

Kudzichepetsa ndi kuopa Yehova ndiko chuma, ndi ulemu, ndi moyo. Miyambo 22:4

Mtima wako usacitire nsanje ocimwa; koma ukhale woopa Yehova tsiku lonse. Pakuti ndithu, pali mapeto; ndipo chiyembekezo chako sichidzadulidwa. Miyambo 23:17-18

Nati kwa oweruza, Yang'anirani chimene muchita; Cifukwa cace tsono kuopa Yehova kukhale pa inu; cenjerani, nicicite, pakuti palibe colakwa kwa Yehova Mulungu wathu, kapena kukondera, kapena kulandira mtulo. 2 MBIRI 19:6-7